

**Sitepe Yachitatu: Kupalira  
Kupalira ndinso Kasamalidwe ka Mbeu**

- Kupalira mofulumira ndikofunikira kwambiri kuti munda umene uli pa ndondomeko ya kakha-koka uchite bwino.
- Palirani koyamba pamene chimanga chatha masabata atatu komanso palirani kachiwiri pamene chimanga chatha masabata asanu.

Ndikufunikira kwambiri kutha kusiyanyitsa pakati pa udzu wongomera m'munda ndi udzu wa "desmodium" (Chithunzi chachisanu n'chimodzi komanso chachisanu ndi ziwiri).



Fig 6. Chithunzi chachisanu ndi chimodzi: Timbande ta Desmodium ta miyezi itatu komanso ta miyezi isanu



Fig 7. Chithunzi cha chisanu ndi chiwiri: Kuzulira timbande ta desmodium todzalidwa pakata pa mizere ya chimanga


Chithunzi chachisanu: Kapangidwe ka timizere ta njere za "desmodium" (Fig 5)

- Sakanizani njere za "desmodium" ndi feteleza wa nthakae (pafupifupi chikhatho chimodzi cha njere za "desmodium" zisakanizidwe ndi zikhatho ziwiri za fetelezayu)
- Kilo imodzi ya njere za "desmodium" imafunikira pa munda wokwana ekala imodzi.
- Ngati simungakwanitse kupeza feteleza, sakanizani njere za "desmodium" ndi mchenga wosefeka bwino, kenako fesani mu timizere tomwe mwakumba ndi ndodo tija ndipo fotserani ndi kadothi pang'ono. (Onani chithunzi chachisanu m'musimu).
- Udzu wa "desmodium" udzalidwenso pa mzere wa m'mapeto omwe mwadzala chimanga ndipo udzuwu udzalidwe pa masentimita 37.5 (37.5cm) kuchoka pa phando.

Dalani udzu wa "desmodium" ndi mvula yoyambilira kuti njere zake zimere bwino.



CHICHEWA – MALAWI



**FARMERS' GUIDE ON  
PLANTING A PUSH-PULL FIELD**

Mukafuna kudziwa zambiri, Lemberani ku:  
Total LandCare (Push-pull Project),  
P. O. Box 2440, Lilongwe, Malawi,  
Telephone: 01 770 904/905.  
E-mail: total.land.care@gmail.com

International Center of Insect Physiology and Ecology (ICIPE), Kenya with Rothamsted Research, UK, Kenya Agricultural Research Institute (KARI) and Ministry of Agriculture (MOA), Kenya

**Donors:**

Kilimo Trust East Africa, Biovision Switzerland and European Union

Visit website: [www.push-pull.net](http://www.push-pull.net)

**M**u ndondomeko ya “push-pull” udzu wa Senjere umadzalidwa mozungulira munda wa chimanga chomwe chadzalidwa mmunda kuchita ngati msampha wokolera tizilombo koma uli udzu. Udzu wa senjerewu umaitana tizilombo tonga ngati mbozi tochedwa “stemborer pachingerezi” kochokera m’ munda wa chimanga uja. Tizilomboti timadzaikira madzira ake mu udzu wa Senjerewu koma udzuwu suumakwanitsa kusamalira tiana tomwe tizilomboti timaswa kotero kuti sitikhala moyo. Udzu ochedwa “desmodium” pachingerezi umadzalidwa pakatikati pa mizere ya chimanga. Udzu wa mtunduwo umatulutsa fungo lomwe tizilombo tokhala ngati mbozi tija sitilikonda ndipo tizilomboti timathawa. Udzu wa “desmodium” umaonjezeranso chonde m’ nthaka komanso umaletska kaufiti kuti asamere kapena kuphatikizana mizu yake ndi ya chimanga. Kotero, chimanga chimatetezeka ku tidzilombo toonongati komanso udzu wa kaufiti zikakhala kuti mundawo wadzalidwa mwandondomeko yotereyi yomwe imachedwa kuti Kankha-Koka “Push-Pull pachingerezi”.

**TINGADZALE BWANJI POTSATIRA NDONDOMEKO YA KANKHA-KOKA**

**Sitepe Yoyamba: Kukonza Munda**

- Sosani munda wanu m’nyengo ya dzuwa
- Limani motembenuza nthaka mpaka pansi kwambiri ndikuphwanya mabuma kukhala mvula isanayambe kugwa.
- Udzu wa “desmodium” umakhala ndi njere zing’ onozing’ono; choncho, donthi likuyenera likonzedwe bwino lopanda mabuma.
- Chitani malire a mapoloti anu pamene mukufuna kuchita ndondomeko ya kankha-koka kuti muthe mudzala mizere itatu ya Senjere kuzungulira m’ malire monse. Onani chithunzi pansipa:




Fig. 1 Chithunzi choyamba: Mmene mungakonzere poloti yanu ya ndondomeko ya push-pull

**Sitepe Yachiwiri: Kudzala**

**Kudzala Udzu wa Senjere**

- Dzalani udzu wa Senjere wa mtundu wotchedwa “Bracharia” pachingerezi m’ malire mozungulira munda wanu wa chimanga
- Dzalani mizere itatu ya senjere mozungulira munda wanu wonse wachimanga. Kutalikirana kwa mizere ya Semjereyi ikhale masentimitala 75 komanso maphando a udzu wa Senjerewu atalikirane masentimitala 75 (75 cm) Onani chithunzi chachiwiri pansipa:




Fig 2.

Chithunzi chachiwiri: Kutalikirana kwa maphando a udzu wa tsekera

- Thirani supuni yaing’ono kwambiri ya fetereza wa nthaka kapena zikhatho ziwiri za manyowa okonzedwa ndi kupsa bwino pa phando lililonse lomwe mukudzala udzu wa senjere.
- Dzalani njere za udzu wa senjere kapena mfundo zitatu za unduzuwu ndipo onetsetsani kuti mfundo ziwiri zakwilirika munthaka, kapena bzalani ziputu zamoyo zomwe zili kale ndi mizu mu mapando ndikufotsera. Onani chithunzi chachitatu pansipa (Fig 3):




Fig 3. Phando limene akufuna kudzala tsekera

- N’udzu wa “Desmodium” ukuyenera udzalidwe moyenera kuti mizere yake izikhala pakati pa mizere ya chimanga. Chimanga mzere umodzi kenako mzere winawo udzu wa Desmodium osati zonse pa mzere umodzi ayi. Izi ndizothandiza kuti kukonza munda chaka chotsatiracho kusadzakhale kovuta. Onani chithunzi chachisanu pansipa.

**Kudzala Chimanga**

- Dzalani chimanga chanu m’ munda omwe wazunguliridwa ndi udzu wa senjere.
- Onetsetsani kuti mzere woyambilira wa chimanga ndiwotalikirana mita imodzi (1 metre) kuchokera mzere wamkati omwe wadzalidwa udzu wa senjere.
- Mpata wovomerezeka wodzalira chimanga ndi masentimita 75 kuchoka pa mzere umodzi kufika pa unzake ndipo masentimita 25 (25cm) kuchoka pa phando limodzii kufika pa phando lina.
- Thirani supuni yaing’ono imodzi ya fetereza nthaka pa phando lililonse.




Fig 4. Chithunzi chachinayi: Kadzalidwe ka chimanga ndi udzu wa desmodium m’ munda

**Tingadzale Bwanji Udzu wa “desmodium” mwakasakaniza**

- Udzu wa “desmodium” umadzalidwa pakati pa mizere yachimanga yotalikirana masentimitala 75 (75cm). Pogwiritsa ntchito ndodo yosongoka mbali imodzi, pangani ngati ka mzere kozama masentimitala imodzi kaena awiri (1-2cm) pakatikati pa ma mzere omwe chimanga chidzadzalidwe. (Onani chithunzi chachisanu m’ musimu).